

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

MOYO WAKO UDZAFUNIDWA

Nkhaniyi yatengedwa pa Luka 12:16-21

Munthu wina, wachuma ndiponso wolemera mu zinthu za dziko lino lapansi, anaganizira za tsogolo lake. Munda wake unakololanso bwino kwambiri ndipo iye anali ndi dzinthu dzochulukuka. Polingalira za chuma chake, anayamba kupanga mapulani akuti agwetse nkhekwe zake kenaka ndi kumanganso zina zazikulu zokwanira kusungamo katundu wake wochulukuka. Polingalira za mtsogolo, iye anati mumtima mwake, “ndagwira ntchito molimbika ndi mwakhama, ndipo panopa ndidyerere chuma changa. Ndili nazo ndalama zochulukuka zakuti zikhoza kunditengera zaka zochulukuka. Ndipuma ntchito ndipo ndidzingodyerera, kumwerera ndi kusangalatsa mtima wanga.”

Ali mkati molingalira ndi zinthu zimene anakwaniritsa kuchita komanso mapulani ake akutsogolo, Mulungu wakumwamba, wolenga dziko lonse analankhula iye nati: “Wopusa iwe, usiku womwe uno udzafunidwa moyo wako; ndipo zinthu zimene unazikonza zidzakhala za yani?”

Munthuyu anafa usiku womwewo ngakhale anali ndi madalitso ake apansipano ndiponso mapulani ake akuluakulu. Chuma chake ndi kudziwika kwake sizikanatha kumulankhulira pamene iye anaima pakhome la moyo wosatha ali wosakonzeka kuima pamaso pa mpando wakuweruza wa Mulungu. Mawa lakelo silinabwere, popeza mu imfa iye anali atayamba moyo wosabwerera wopita ku mdima ndi masautso.

Mulungu anamutchula munthu uja kuti wopusa chifukwa amapanga mapulani ake a zinthu za m'moyo uno koma sanaganizire zokonzekera za moyo wake pamene akuyembekeza moyo wosatha. Kodi munthuyu akupereka uthenga wotani kwa ife lero kuchokera kuseli kwa manda?

“Musamuiwale Mulungu. Woyo wosatha ndi weniweni. Mukafa, sikuti amenewo ndi mapeto, ndi mayambiriro chabe.” Kumwamba ndi malo okongola kwambiri ndi amtendere komanso achimwenwe ndipo kukudikira anthu oyera mtima. Pamene ku gehena, ndi malo a masautso komanso chizunzo ndipo kukudikira anthu ochimwa. Kodi zinthu za dziko lino lapansi zomwe zili zakanthawi zili ndi phindu lanji pamene moyo wosatha ukugogoda

pa khomo lathu? Imfa siilabadira za munthu. Anthu onse, kaya ndi ana, okalamba, olemera, osauka, ophunzira, osaphunzira, odziwika ndi osadzikwika onse adzafa nakaimira pamaso pa Mulungu. Zinthu zimene dziko lino lapansi limaikapo mtima sizidzanunkha kanthu m'moyo uli nkudzawo. Chinthu chimene chidzawerengeredwe ndi chakuti ngati mutambenuka kusiya tchimo lanu, ndipo munalandira Yesu Khristu kukhala mpulumutsi wanu, ndipo tsiku ndi tsiku mukuyenda m'moyo wanu mukutsogozedwa ndi iye.

Anthu akutaya nthawi ndi mphamvu zochulukuka pofunafuna chuma, ulemerero, maphunziro ndi zosangalatsa za thupi. Zisankho zimene amapanga ndi za “lero komanso panopa” osalabadira kuti kodi moyo wao wamuyaya udzakhala wotani. Mulungu waiwalidwa ndi mtundu wa anthu ndipo anthu akungokhala moyo wa nthawi imeneyo.

Mbale wanga, moyo wosatha uli mtsogolomo—ndipo ndi chinthu chimene chilichonse sichidzatha kumeneko komwe nthawi siwerengedwa, popeza ilibe malekezero. Kodi muli okonzeka kukumana ndi Mulungu amene adzaweruze mmene inuyo munachitira ndi moyo wanu? Kumene mumachokera, chuma chanu, kudziwika kwanu, mpingo wanu kapena chipembedzo chimene mumakhulupirira zonsezi sizingathe kukuwombolani ku mphamvu za mdima wosatha. Mukuyenera kulandira Yesu Khristu ndipo tsiku lililonse muyende mu moyo wachiyero pamaso pa Mulungu.

Mneneri Amosi analimbikitsa aliyense mnthawi yake kuti, “dzikonzeretu kukomana ndi Mulungu wako” (Amosi 4:12). Wolemera uja anali atakonzekera bwino chuma chimene adzadye atapuma pantchito, ndipo panalibe

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Zinthu zimene dziko lino lapansi limaikapo mtima sizidzanunkha kanthu m'moyo uli nkudzawo.”

Mau a Mkonzi

Kalozera wa Baibulo

Kulapa Kwa Mu
Baibulo

Funso Yanko:
Kubwezera

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

cholakwika chilichonse ndi zimenezo, koma vuto linali lakuti mu mapulani ake onse sanakonzekere kukumana ndi Mulungu. Kukonzekera kumatanthauza “kuonetsetsa kuti zonse zili bwino”. Kodi mwakonzekera kukumana ndi Mulungu? Kodi mukukhala moyo uno pokumbukira kuti kuli chiweruzo ndi moyo wosatha? Zimatengera kuikapo khama pofuna kukonzekera chinachake. Chisankho cha tsiku lililonse la moyo wanu mudzichipanga pofuna kukondweretsa



“Chisankho cha tsiku lililonse la moyo wanu mudzichipanga pofuna kukondweretsa Mulungu ndiponso kuti moyo wanu udzafikire pabwino.”

Mulungu ndiponso kuti moyo wanu udzafikire pabwino.

Zoona zake zimene zili zokhumudwitsa nzakuti anthu ambiri sakulabadira za moyo. Ambiri amadziwa za Mulungu komanso mwina za maonekedwe a chipembedzo, komabe zisankho zao zimakhazikika pa zinthu zimene zikhoza kupititsa patsogolo moyo wao wapansi pano osati chimene chingawathandize kwambiri kuuzimu. Nanga inuyo mumatani?

Moyo ndi wosapanganika, ndipo palibe wina aliyense wa ife amene amadziwiratu tsiku limene adzafe ndi kukakumana ndi Mulungu.

Tisakhale m'moyo wa munthu

wopusa. “Pakuti munthu adzapindulanji, akalandira dziko lonse, nataya moyo wake? Kapena munthu adzaperekanji chosintha ndi moyo wake?” (Mateyu 16:26). Pamene tafa ndikukaimirira pampando wa kuweruza, koma m'moyo uno osamuika Mulungu patsogolo, kodi tidzafunafuna kuti tisinthanitse ndi chiyani kuti tipeze moyo wosatha? Tikhoza kupereka chilichonse komanso kenakalikonse kuti tipulumuke ku chizunzo cha Gehena. Tikakafika ku moyo wosatha, moyo uliwonse udzafunitsitsa kuyambanso moyo wina atati apatsidwe mpata umenewo. Iwo akhoza kulolera kusintha ndi kutaya china chilichonse chimene chikhoza kuwasokoneza kuti asakhale moyo wolungama ndi waumulungu. Iwo akhoza kusiyana nazo zonse kaya ndi chuma, maphunziro, zosangalatsa moyo ndi zikhalidwe zina zimene zinkawasiyanitsa ndi Mulungu. Komabe, zoona zake nzakuti sitibwerezanso tikafika ku moyo wosatha. Moyo nkamodzi basi. Lero ndiyo nthawi yanu, ndipo uno ndiye mwai wanu.

Kodi muchita chiyani ndi moyo wanu tsopano lino? Ngati mukukhala chifukwa cha zinthu za dziko lapansi koposa kukhala tsiku lililonse kutumikira Mulungu ndi kupereka chiyembekezo ku dziko lino, mukufunika kuti mudzichepetse mtima wanu ndipo mupemphere. Muvomereze Yesu mu mtima mwanu ndipo mulole kuti chisankho chilichonse chimene mungapange chisalamulidwe ndi dziko lapansi koma ndi dziko lamuyaya limene likubwera posachedwapa. Nthawi yatsala pang'ono ndipo Yesu akukudikirani! ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kutu mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Ndipo anatuluka, nalira misozi ndi kuwawa mtima. — Luka 22:62

Pamene Yesu anali kuyesedwa, Petro, amene ankamutsatira kuchokera chapatali potero, anamukana Ambuye katatu konse. Pambuyo pake, Petro anatuluka panja nakalira kwambiri. Mtima wake unali wosweka ndipo anali ndi chisoni kwambiri chifukwa iye anakana Mbuye wake ndi mpulumutsi wake. Ubwino wa nkhanayi ndi wakuti sizinathere pomwepa. Yesu atauka kuchokera kwa akufa, Iye anafunitsitsa kwambiri kuti uthenga umufike Petro wakuti Iyeyo wauka. Ngakhale kuti Petro anamukana Ambuye wake, Mulungu anamulandira chifukwa cha mtima wake wolapa ndipo Petro anakhalanso ndi mwai wina wotumikira Yesu. Ulemerero upite kwa Mulungu!

Nkhani imene tikulingalira ulendo uno uli pa mutu wa Kulapa kuchokera mu baibulo. Ngakhale kuti pali kulapa kuyambira padziko, pabanja komanso pampingo, nkhanayi makamaka ikukhudza chiphunzitsa cha Kulapa kokhudza munthu. Ndikuganiza kuti pakhoza kukhala chisoni chochuluka chifukwa cha tchimo limene lachitidwa. Anthu ali m'avuto ndipo akutembenukira ku zinthu za dziko lino pofuna kupeza mayankho amene sathandiza. Yankho lake likupezeka pa kugwada pa maondo ndipo ndi kukhala ndi mtima wachisoni wofunafuna Mulungu kuti akhululukire.

Pamene pali kulapa kwa munthu, mabanja adzayanjananso, maubale adzabwezeretsedwa, zolakwika zidzakonzedwa ndipo chiyero chidzachita ufumu. Zinthu zimenezo zikasowa ndi chifukwa chake anthu samamva chisoni chowafikitsa pakulapa. Mabungwe a chikhristu amalalikira Khristu, koma iwo sanena zokhudza kulapa. Atumiki a Mulungu enieni sakuyenera kubwerera m'buyo pa kulalikira kwa oipa za kufunikira kwakulapa. Anthu amafuna madalitso a Mulungu, koma kawirikawiri samakhala okonzeka kulipira dipo lake kuti awalandire. Pali chimene chimachitika chomwe chimaposa kungokhala ndi mapemphero a tsiku ndi tsiku opempherera kukhulukidwa kwa machimo. Kodi tilalikire zakuti titembenuke ku uchimo kenaka nkubwereranso ku zinthu zomwezo zimene tinazitaya? Ayi zisatero. Tisiyane ndi uchimo, ndipo pali mphamvu mu mwazi wa Khristu yakuti tikhoza kukhala mu moyo wachigonjetso pa mphamvu ndichikoka cha uchimo.

Ndimadalitsika ndikamaona anthu akupempherera chipulumutso ndipo ndimakhala okondwa kumva anthu akuyambanso moyo watsopano wotsata Mulungu, komabe kawirikawiri zimenezi sizifika kumapeto. Ndikhulupirira kuti pamakhala kuti palibe kulapa. Tikuyenera kumvetsetsa kuopsa kwa uchimo ndi kusamvera ndipo mwachisoni tisiyane nazo. Mwachimwemwe tikuyenera kumamatira kwa Mpulumutsi. Tidzalandira chipulumutso chokhalitsa chimene chimapangitsa kuti tisiyane nalo tchimo kwathunthu.

Ngati mukuchimwa, ndiye kuti simunapulumsidwe. Kaya ena amaganiza bwanji za moyo wanu wauzimu, inuyo mumadziwa ndithu ngati muli ochimwa, ngati munabwerera mmbuyo, ngati muli wachiphamaso komanso ngati muli woyera wa Mulungu. Ngati mukudziwa kuti chikumbumtima komanso mtima wanu siwoyera pamaso paMulungu, ndikukudandaulirani kuti muyigwiritse ntchito nthawiyi kuti mulape. Tembenukani kusiya uchimo umene wakuzingani ndipo perekani moyo wanu ndi mtima wanu kwathunthu kwa Ambuye. Iye adzakhala wokhulupirika kukuthandizani kuti mukhazikike ndikukula mu uzimu wanu. Lapani lero nthawi isanathe. Pempherani.

Michael W. Smith

October 2021

NDIPO ANTHU ANGA OTCHEDWA DZINA LANGA
AKADZICHEPETA, NAKAPEMPHERA, NAKAFUNA NKHOPE YANGA,
NAKATEMBENUKA KULEKA NJIRA ZAO ZOIPA;
PAMENEPO NDIDZAMVERA M'MWAMBA,
NDIKUKHULULUKIRA CHOIPA CHAO, NDIKUCHIRITSA DZIKO LAO.

-2 MBIRI 7:14



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.



Kalozera powerenga Baibulo

Mutu: Kulapa

Kuwerenga Malemba: Chifukwa chake lapani, bwererani kuti afananizidwe machimo anu. — Machitidwe 3:19

Matanthauzo: Kulapa: Kusintha kwa maganizo a munthu, pofuna kukonza zinthu, makamaka podana kotheratu ndi machimo ake akale. (Thayer's Greek Lexicon).

Kulapa: Kusweka mtima kapena kumva chisoni chifukwa cha zoipa zimene zinachitidwa m'mbuyomu kumene kumatsagana ndi kusinthika kwa malingaliro amene amakhudzana ndi kutembenuka ndi kusiyana nalo tchimo kenaka ndi kuyang'ana izo zimene zimakondweretsa Mulungu.

Chidule: Ochimwa onse akuitanidwa ndi Mulungu kuti alape andi kutembenuka kusiya machimo awo. Uthenga wopezeka mu uthenga wabwino Ndiwo wakuti munthu adane ndi kusiyana nacho chisapembedzo chonse kenaka ndi kutsatira Yesu mu chiyero. Popanda kulapa palibe pochipulumutso chenicheni.

I. Ndani ayenera kulapa?

- A. Mateyu 9:12-13 Ochimwa.
- B. Machitidwe 17:30 Anthu onse paliponse.

II. Ulaliki wa kulapa

- A. Luka 3:3 Yohane Mbatizi—Kulapa kuti machimo akhululukidwe.
- B. Marko 1:14-15 Yesu—Lapani ndi kukhulupirira uthenga wabwino.
- C. Marko 6:12 Ophunzira—Anthu akuyenera kulapa.
- D. Machitidwe 20:20-21 Paulo—Kulapa kuyang'ana kwa Mulungu.

III. Kufunikira kwa kulapa

- A. Luka 13:3 Pokhapokha mutalapa, mudzaonongeka.
- B. Machitidwe 3:19 Kutu machimo anu afufutidwe.
- C. Chivumbulutso 2:5 Kutu mulandire madalitso ndikudzoza kwa Mulungu.

IV. Chipatso cha kulapa

- A. Luka 3:8 Onetsani zipatso zosonyeza kulapa.
- B. Machitidwe 26:19-20 Chitani ntchito zosonyeza kulapa.
- C. Yakobo 4:8 Sambani m'manja mwanu inu ochimwa.

V. Chizindikiro cha kulapa: Chisoni

- A. 2 Akorinto 7:9-11 Chisoni cha umulungu chimabweretsa kulapa.
- B. Masalmo 51:17 Mtima wosweka ndi wogonja.

VI. Chizindikiro cha kulapa: Kuvomereza machimo

- A. 1 Yohane 1:9 Ngati tivomereza machimo athu.
- B. Miyambo 28:13 Aliyense amene avomereza tchimo ndi kulileka.

VII. Chizindikiro cha kulapa: Kusiya tchimo

- A. Yesaya 55:6-7 Wochimwa asiye njira yake yoipa.
- B. Ezekiele 18:30 Lekani mphulupulu zanu zonse.

VIII. Chizindikiro cha kulapa: Kudzipatula ku kusakonda zaumulungu

- A. 2 Akorinto 6:14-18 Dzipatuleni.
- B. Ezekiele 14:6 Mutembenuke kusiya mafano anu

IX. Chizindikiro cha kulapa: Kubwezeretsa

- A. Levitiko 6:4-5 Bwezeretsani zimene zinatengedwa.
- B. Luka 19:8-9 Zakeyu anabweza zimene analanda.

X. Zitsanzo za kulapa

- A. Luka 15:21 Mwana wolowerera—“Ndinachimwira kumwamba.”
- B. Luka 18:13 Wokhometsa msonkho—“Mulungu mundichitire chifundo ine wochimwa.”
- C. Yona 3:8 Nineve —“Abwere yense kuleka njira yake yoipa.”

XI. Kuitanidwe kuti tilape

- A. Machitidwe 2:37-40 Lapani...Dzipulumutseni nokha.
- B. Chivumbulutso 3:19 Poto chitani changu, ndipo mulape.

XII. Mwai wa kulapa

- A. Chivumbulutso 2:21 Mulungu anatipatsa mwai wakuti tilape.
- B. 2 Akorinto 6:2 Lero ndilo tsiku la chipulumutso.
- C. Aroma 2:4 Ubwino wa Mulungu.
- D. 2 Petro 3:9 Yehova safuna kuti wina aliyense awonongeke.


Kumaliza

Ndinena kwa inu, kotero kudzakhala chimwemwe Kumwamba chifukwa cha wochimwa mmodzi wotembenuka mtima, koposa anthu olungama makumi asanu ndi anai mphambu asanu ndi anai, amene alibe kusowa kutembenuka mtima. — Luka 15:7

KULAPA

KWA MU BAIBULO

Tembenukani kuchoka ku uchimo, kanani choipa, ndipo mupulumutsidwe mwamphamvu ya Mulungu. Paliponse pamene uthenga wa Yesu Khristu ukulalikidwa, uthenga wa kulapa kwenikweni ukuyenera kunenedwa; popeza popanda kulapa, palibe chipulumutso chenicheni.



“Kulapa kumatanthauza kubweza chimene chimachitika kapena kusintha njira.”

Kutembenuka

Kulapa kumachitika pamene wina akumva chisoni ndi machimo ake akale ndipo afulatira zoipa natembenuka ndikuyamba kutsata Khristu. Zimenezi zimakhudza kutembenukira ku icho chimene chili choipa ndipo ndikupanga chisankho kuti musabwererekonso. Kulapa kumatanthauza kubweza chimene chimachitika kapena kusintha njira. Mipingo yambiri yachikhristu ikulalikira Yesu Khristu ngati wochita chopepesera machimo koma sakulalikira uthenga wakulapa. Ndi chinthu chimodzi kulandira

Khristu, koma ndi chinthu chinanso kusintha ndikusiya zinthu izo zimene sizikondweretsa Mulungu. Ngakhale kuti chipulumutso sichibwera chifukwa cha ntchito zabwino koma ndi mphatso yochokera kwa Mulungu, nafenso ngati anthu tili ndi mbali yakuti tichitepo. Mtumwi Petro anawauza anthu kuti, “Chifukwa chake lapani, bwererani kuti afafanizidwe machimo anu” (Machitidwe 3:19). Mulungu adzakhululukira anthu okhawa amene ali siliyasi ndi chipulumutso chao mwakuti ali okonzeka kusiya zosakondweretsa Mulungu zilizonse.

Yesu anabwera kudzikilo lino lapansi ndipo anafera machimo a anthu kuti iwo onse akhoza kupulumutsidwa. “pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu” (Aroma 3:23). Yesu anabwera kudzaitana “ochimwa kuti alape” (Mateyu 9:13), ndipo Mulungu “alinkulamulira anthu onse ponseponse atembenuke mtima” (Machitidwe 17:30). Palibe amene sakuitanidwa kuti alape, popeza onse analekanitsidwa ndi Mulungu kudzera mu uchimo ndi kuchita zoipa. Popanda kunyansidwa ndi icho chimene chili

cholakwika ndiponso kusakhala ndi chisoni chimene sichikondweretsa Mulungu, palibepo chipulumutso.

Wofunikira pakulalikira uthenga wabwino

Uthenga wa kulapa sunali uthenga watsiku limodzi umene unalalikidwa pamalo obisika. YohaneMbatizi, amene anali mkupamame wa Khristu, “anadza kudzikilo lonse la m’mbali mwa Yordani, nalalikira ubatizo wakulapa mtima kuloza ku chikhululukiro cha machimo” (Luka 3:3). Yesu analalikira uthenga wabwino wa ufumu wa Mulungu ndipo mau awa omveka bwino: “tembenukani mtima, khulupirirani Uthenga Wabwino” (Marko 1:14-15). Ophunzira anatimidwa ndipo “analalikira kuti anthu atembenuke mtima” (Marko 6:12). Paulo anawachitira umboni “Ayuda ndi Agriki za uthenga wa kutembenuka mtima kulinga kwa Mulungu, ndi chikhulupiriro cholinga kwa Ambuye wathu Yesu Khristu.” (Machitidwe 20:21). Uthenga uwu ndi wosiyana kwambiri ndi uthenga wosavuta wakuti anthu akhulupirire mwa Yesu, umene ndi ukhoza kuwapumuza anthu ku udindo wofuna kusintha. Chifukwa cha ichi, mipingo yachinyengo yambiri masiku ano imaphunzitsa kuti sizingatheke munthu kukhala ndi moyo koma osachimwa. Mphamvu yeniyeni ya uthenga wabwino ndiyo yakuti kudzera mu kulapa ndiponso kukhulupirira kwa Khristu, pali mphamvu yakuti tikhoza kupita koma “osakachimwanso” (Yohane 8:11). Mulungu sadzavomera china chilichonse chochepera apa, popeza popanda chiyeero “palibe mmodzi adzaona Ambuye” (Ahebri 12:14).

Kuli koyenera pa chipulumutso

Kulapa ndi gawo lofunikira kwambiri la chipulumutso kuti munthu akhale ndi moyo wosatha. Yesu ananena pa Luka 13:3 kuti, “Iaitu; koma ngati inu simutembenuka mtima, mudzaonongeka nonse momwemo” sikokwanira kulowa nawo mu gulu lachipembedzo ndi kungolambira Ambuye ndi chikhululukiro chooneka ngati chaumulungu. Pakuyenera kukhala kusintha kwenikweni kwa moyo umene umayamba ndi kulapa kwa munthuyo. Imeneyo ndiye njira yokhayo yomwe uchimo ukhoza kufafanizidwa (Machitidwe 3:19). Pokhapokha iwo atalapa, kudzoza ndiponso madalitso a Mulungu adzachotsedwa kwa anthu komanso mipingo imene yabwerera mmbuyo ndi kugwa. Chimenechi ndi chitsanzo chomwe chikuperekedwa mu kalata yaku mpingo wa ku Efeso pamene akuti: “Potero kumbukira kumene wagwerako, nulape, nuchite
(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)

ntchito zoyamba; koma ngati sutero, ndidzadzwa kwaiwe, ndipo ndidzatunsa choikaponyali chako, kuchichotsa pamalo pake, ngati sulapa” (Chivumbulutso 2:5).

Yohane Mbatizi anawachenjeza Afarisi kuti, “Chifukwa chake balani zipatso zakuyenera kulapa mtima, ndipo musayambe kunena mwainu nokha, Atate wathu tili naye ndiye Abrahamu” (Luka 3:8). Udindo ndi kudziwika

sizipangitsa kuti wina aliyense asafune kulapa. Pali anthu mu maudindo a ulamuliro mu mabungwe a chipembedzo ndipo iwo akuyenera kuti adzichepetse mitima yao nalilire kwa Mulungu. Abusa, oimba ndi aphunzitsi adzaonongeka

ndi kutaya miyoyo yao ngati sakhala ndi kusweka mtima kwenikweni natembenukira ku uchimo wao wochitika pamene ali paokha kapena anthu akuona.

Ntchito za Kulapa ndizo udindo wathu—kusintha mtima ndi maganizo ndi kuyamba kutsata kudzera mu mau ndi mu ntchito “kuti alape, natembenukire kwa

Mulungu, ndikuchita ntchito zoyenera kutembenuka mtima.” (Machitidwe 26:20). “Sambani m’manja, ochimwa inu” (Yakobo 4:8), ndipo tembenukani ndipo yang’anani kwa Ambuye kuti mupulumuke.

Chisoni cha umulungu

Chisoni cha umulungu ndi mfundo yofunikira kwambiri ya kulapa imene imabweretsa chipulumutso. “Pakuti chisoni cha kwa Mulungu titembenezira mtima kuchipulumutso, chosamvetsanso chisoni; koma chisoni cha dziko lapansi chichita imfa. Pakuti, taonani, ichi chomwe, chakuti mudamvetsedwa chisoni cha kwa Mulungu, khama lalikulu lanji chidalichita mwainu, komanso chodzikonza,” (2 Akorinto 7:10-11). Nzochita kuonekeratu kuti chisoni cha umulungu nchoposa chisoni cha dziko lapansi pamene munthu asowa mtendere chifukwa wachita choipa komabe apitirira kuyenda mnjira ya kusamvera. Chisoni cha umulungu ndi chozama, ndipo ndi mtima wosweka umene umabweretsa kusintha. Mulungu adzavomera ndikulandira chisoni choterocho ndi kudzichepetsa popeza “Nsembe za Mulungu ndizo mzimu wosweka ndi wolapa” (Masalmo 51:17).

Vomerezani ndi kuzileka

Kulapa kumakhudza kuvomereza ndi kunena mosabisa tchimo limene munthuwe wachita. Popanda kuvomereza machimo palibepo chikhululukiro. Pa 1 Yohane 1:9 akunena kuti: “Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndikutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse.” Komabe, “Wobisa machimo ake sadzaona mwai; koma wakuwawomereza, nawasiya adzachitidwa chifundo” (Miyambo 28:13).

Kuvomereza uchimo koma osauleka ndi chinthu chachabe ndi chopanda pake. Malemba akunena motsindika

pa mfundo imeneyi kuti, “Woipa asiye njira yake, ndi munthu wosalungama asiye maganizo ake, nabwere kwa Yehova; ndipo Yehova adzamchitira chifundo; ndi kwa Mulungu wathu, pakuti Iye adzakhululukira koposa” (Yesaya 55:7). Ngakhale mu Chipangano Chakale, mneneri anawauza anthu kuti “Bwererani, nimutembenukire kuleka zolakwa zanu zonse, ndipo simudzakhumudwa nazo, ndikuonongeka nayo mphulupulu” (Ezekiele 18:30). Tchimo lidzakhalabe chinthu chokuonongani ngati simutembenuka kuchoka ku mphulupulu yanu.

Mfundo ina ya kusiya tchimo ndiyo kulapa mwakuti kulekana nalo ntchito kuchokera ku chisapembedzo chilichonse ndiponso zikhaliidwe zonyansa. Paulo analangiza mpingo wa ku Korinto kuti udzipatule ku kuphatikana ndi osakhulupirira, kupembedza mafano ndi chidetso chilichonse (2 Akorinto 6:14-18). Chimodzimodzinsu, Ezekiele anawalangiza Aisraele kuti, “lekani mafano anu, tembenuzani nkhope zanu kuzisiya zonyansa zanu zonse” (Ezekiele 14:6). Kulapa kumafunikabe kuti munthu asiyaneni ndi mafano a masiku ano a chuma, mavalidwe atsopano, masewero, zinthu zosangalatsa ndi zina zomwe zimatakasa mitima ndi maganizo a anthu.

Konzani zinthu zikhale bwino

Kubwezeretsa ndi chikhaliidwe kapena chipatso china cha Kulapa. Pamene Zakeyo analonjeza kuti adzabweza ndalama kwa iwo amene anawalakwika, Yesu anayankha nati, “Lero chipulumutso chagwera nyumba iyi” (Luka 19:8-9). Kubwezeretsa ndiko kukonza zolakwika zakale ndipo zimaonetsa mzimu weniweni wa kulapa umene umapangitsa kuti munthu achitepo kanthu.

Malemba amapereka chithunzithunzi chokoma cha kulapa kwenikweni. Mwana wolowerera analankhula nati, “Atate ndinachimwira Kumwamba ndi pamaso panu, sindiyeneranso konse kutchulidwa mwana wanu.” (Luka 15:21). Wokhometsa msonkho pamene amapemphera mu kachisi analungamitsidwa, popeza iye sanathe kukweza maso ake kumwamba ndipo analirira kwa Mulungu kuti, “Mulungu, mundichitire chifundo, ine wochimwa” (Luka 18:13). Chifundo cha Mulungu chinafikira kwa mzinda woipa wa Nineve pamene analapa ndipo anatembenuka nasiya njira zao zoipa (Yona 3:8). Mulungu ndi wachifundo ndipo amapereka mpata kwa wochimwa kuti alape (Chivumbulutso 2:21) ndipo amawalandira iwo mwachimwemwe chachikulu ndikusangalala kumwamba (Luka 15:7). Mulungu “aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa.” (2 Petro 3:9).

Lapani lero!

Tsiku lina kuleza mtima kwa Mulungu kudzathera mu chiweruzo. Uthenga wa Petro pa tsiku la Pentekoste wakuti, “Lapani, batizidwani yense wa inu m’dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu” (Machitidwe 2:38), ukadali wofunikira ngakhale mu mbadwo walero. Ngati simunalape kwathunthu, “Tsopano ndiyo nyengo yabwino yolandiridwa, taonani, tsopano ndilo tsiku la chipulumutso” (2 Akorinto 6:2). Pali mtendere ndi mpumulo wodabwitsa umene umabwera ndi kulapa kwenikweni. ■



“Kulapa

kumafunikabe kuti

munthu asiyaneni

mafano a masiku

ano ...zomwe

zimatakasa mitima

ndi maganizo a anthu.”



“Sikuti ntchito yachipulumutso ya Mulungu inali yosakwanira, kunali kusoweka kwa kulapa chisanabwere chipulumutso.”

Kodi kulapa kuli ndi phindu lanji pa chipulumutso?

Kunena mwatchutchutthu, kulapa kumalumikizana ndi chipulumutso mu malemba. Yesu anati “tembenukani mtima ... khulupirani Uthenga Wabwino.” (Marko 1:15). Mulungu anakonza kuti tikhoza kulandira chipulumutso chathu kudzera mu imfa a Yesu pamtanda. Iye ali wofuna ndi wokonzeka kutikhululukira ife machimo athu komanso kutipatsa mphatso ya moyo wosatha. Komabe mphatso imeneyo imaperekedwa

“anthu amene amafunafuna chipulumutso popanda kulapa kwenikweni amasautsika ndi zochitika m’ moyo wao.”

kwa okhawa amene akumva chisoni chifukwa cha zoipa zao ndipo mwakufuna kwao apanga chisankho kuti atembenuke kuchoka ku machimo ao.

Iwo amene amafunsa Mulungu za chipulumutso koma mwa iwo mulibe

kulapa kwa umulungu, sangakhale ndi moyo weniweni wosinthika. Pamwamba pa zonse pakuyenera kukhala chikhumbokhumbo chofuna kusiya tchimo ndi kutsatira Khristu. Yesu anamuuzako munthu wina wachinyamata koma ali olemera amene amafuna kumutsata kuti poyamba apite akagulitse zonse zimene ali nazo. Kumvera kwa munthu ameneyu kukanakhala mphatso ya kulapa ndiponso chionetsero chakuti iye amafuna kusiya zonse chifukwa cha Khristu. Tsoka ilo, munthu wachinyamatayu sanali wokonzeka kutembenuka ndi kusiya zinthu za dziko lino lapansi.

Nthawi zambiri anthu amanena kuti amakhulupirira mwa Yesu Khristu, komabe napitirira mu machimo ao. Anthu awa sali wopulumutsidwa kwenikweni, popeza chipulumutso chimaperekedwa kwa iwo amene ali ndi mtima wolapadi. Pakhoza kukhala kusintha kwa zokhumba, koma anthu amene amafunafuna chipulumutso popanda kulapa kwenikweni amasautsika ndi zochitika m’ moyo wao. Pakuyenera kukhala kuvomereza kwa choipa chimene munthu wachita ndiponso chisoni cha umulungu chifukwa cha kusakondweretsa Mulungu. Pakuyenera kukhala chilakolako chofuna kusiya tchimo lakale, popeza ngati zimenezi sizichitika, machimo omwe aja adzabwereranso. Anthu amaganiza kuti ntchito ya Mulungu ya chipulumutso inali yosakwanira.

Sikuti ntchito yachipulumutso ya Mulungu inali yosakwanira, koma kunali kusoweka kwa kulapa chisanabwere chipulumutso. Nchifukwa chake kulapa kuli kwaphindu kwambiri ngati munthu akufuna kupulumutsidwa, popeza popanda kulapa munthu sangathe kupulumutsidwa kwathunthu ku mphamvu ya uchimo.

Choyamba wochimwa akuyenera kuti atsekule mtima wake kwa Mulungu ndipo asiye chisalungamo chonse. Zimenezi zimatsekula njira kwa Mulungu kuti agwire ntchito yodabwitsa ya chipulumutso imene idzamuthandize munthu kuyenda mu moyo watsopano. Chimenechi ndiye chifukwa chomwe Yesu analangiza anthu ochuluka kuti awerengetsere dipo lake. Taganizirani kuti zimatanthauza chiyani pamene munthu wasenza mtanda wake ndi kutsatira Yesu. Lingalirani mozama musanapange chisankho. Pamene mwapanga chisankho chakuti mukufuna kutsatira Mulungu mu kulapa, mutsekule khomo la mtima wanu kuti mulandire chidzalo cha chisomo cha Mulungu cha chipulumutso.

Kodi kumva kuipidwa ndi tchimo langa kuli kofanana ndi kulapa?

Ayi. Munthu wosalapa sangamve chisoni kapena kuona choipa pamene akuchita choipa china chake, komabe sipakhala kusintha kwenikweni. Tangoganizani za mwamuna wankhanza amene amalira namuza mkazi wake kuti akumva chisoni chifukwa amamuzunza panthawi yomwe anali ataledzera. Chisoni chimenecho chimatha pamene waledzeranso, ndipo kenaka amadzachitanso. Chimenecho ndiye chisoni cha dziko lapansi. Chisoni chaumulungu (2 Akorinto 7:10) ndi icho chimene chimamufulumiza ochimwa kuti asinthe posatengera kuti zimupweteka motani. Pamene munthu watsutsidwa ndi Mzimu Woyera, iye akhoza kumva kuwawa mwinanso kulira kumene chifukwa akudziwa kuti akukhala m’ moyo wa uchimo. Komabe, misozi kapena maganizo omwa odzimvera chisoni sizikwanira. Pakuyenera kukhala chisoni chaumulungu chinachake chifukwa chozindikira kuti wachita cholakwa ndipo izi zitsogozane ndi malingaliro osafunanso kubwerera ku moyo wa uchimo. Chimenechi ndiye chisoni chimene chikhoza kubweretsa kulapa.



KODI MUKUDZIWA?

Pamene Yona analalikira ku Nineve kuti mzindawo udzaonongedwa patatha masiku 40, anthuwo anakhulupirira Mulungu ndipo analalikira chosala. Panalibe chamoyo chilichonse mu mzindawo, kaya ndi munthu kapena nyama chimene chinadya kapena kumwa. Anthu ndi nyama zomwe, onse anavala ziguduli kusonyeza kusweka mtima ndi kulapa. Mulungu anauleka mzindawo osawuononga! (Yona 3:4-10).



Mau a Nyengo Yake

UBWINO WA MULUNGU

Kapena upeputsa kodi kulemera kwa ubwino wake, ndi chilekerero ndi chipiriro chake, wosadziwa kuti ubwino wa Mulungu ukubwezera kuti ulape? —Aroma 2:4

Palibe chimene tingachite kuti tithawe chiweruzo cha Mulungu, popeza nzodziwikiratu kuti “ife tonse tidzaimirira kumpando wakuweruza wa Khristu” (Aroma 14:10) ndipo tidzayenera kupereka mndandanda wa zimene tinachita ndi moyo wathu. Komabe Ambuye mwa chifundo akutalikitsa dala nthawi kuti potero anthu akhoza kupulumutsidwa ku mphamvu ya uchimo ndiponso akhale ndi mwai wokonzekera moyo wosatha. Chifundo cha Mulungu chikuwafikiranso ngakhale oipitsitsa mwa anthu oipa, ndipo chikondi chake chimawafikira iwo amene sawerengeredwa pakati pa anthu. Iye amawachitira chifundo woipitsitsa mwa ochimwa, ndipo amasamalira amene ali okanidwa ndi onyozedwa.



Tsono anthu ambiri akupeputsa ubwino wa Mulungu posalabadira za chikondi ndi kuleza mtima kwake ndipo amakana kulandira dongosolo lake labwino la chipulumutso. Zoonadi, ndi ubwino wa Mulungu umene umatsogolera anthu kunyengo yakuti akhoza kulapa. Pamene maso a munthu atsekuka ku chikondi chachikulu cha Mulungu ndi ku mphatso ya moyo wosatha, izi zimafewetsa mtima komanso zimalenga chikhumbokhumbo cha zonse zimene Mulungu wapereka.

Ifeyo sitiyenera kulandira kukoma mtima kumeneko, kuleza mtima, kapena chifundo chifukwa tonsefe tinakhalako ogalukira Mulungu. Ndi mkati mwamoyo wokana Mulungu kotere ku pamene Iye amaonetsera chikondi chake kawirikawiri pothandiza ochimwa panthawi zovuta za moyo wake. Pamene mavuto abwera ngati namondwe, nasautsa, Mulungu amaonetseranso chisamaliro chake. Pamene zochita za anthu zifuula kufuna chiweruzo chifukwa cha kupweteka ndi ululu umene ena owazungulira amawachitira, Mulungu amabwera ndi kupereka chifundo chake ndi kuleza mtima kwake. Iye amachedwetsa chiweruzo chake ndipo amabweza chilango chake chifukwa cha kukoma mtima kwake kopanda malire. Kulemera kwa ubwino wake kumavumbulutsidwa kangapo konse kwa anthu amene ali ochimwa.

Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu ali wabwino chotere kwa anthu amene sawuyenera? Ndi chifukwa cha ubwino wake kumene kumawatsogolera anthu kukulapa (Aroma 2:4). Ubwino ndi chikondi chake ndi zimene zimawakakamiza anthu ndiponso kuwalimbikitsa iwo kuti atembenuke. Zimene zimawatsogolera anthu kuti asiye zolakwa ndikukakamira kuzinthu zimene zimakondweretsa Yehova.

Khomo la chisomo lili lotsekuka ndipo kukhululuka kukudikira mtima wolapa. Tiyamika Mulungu chifukwa cha ubwino wake! ■

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE